# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA MACHINGA M'DZINJA LA 2025-2026

## DZINJA LA 2025/2026 MWACHIDULE

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/2026

Boma la Machinga likuyembekezeka kudzalandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuchepela apo mu dzinjali.


## October 2025




Tiyembekezere nyengo yotentha m`mweziwu. Komabe mvula ya Chizimalupsya ikhoza kudzagwa pa mlingo osaposera 30 mm.

Mvulayi ikuyembekezeka kugwa ndi mphepo ya mkuntho komanso ziphaliwali.


## November 2025




Mvula ya mlingo okhazikika kapena kuchepela apo ikuyembekezeka mmadela ambiri ya mlingo osaposera 50mm.

Mvulayi ikhoza kudzagwa ndi mphepo ya mkuntho komanso mphezi.


## December 2025




Mu December, mvula ya mlingo okhazikika kapena kuchepera apo ikuyembekezeka m'madera ambiri a bomali ya pakati pa 200mm ndi 250mm. Komabe, madera a kwa TA Kawinga ndi SC Chikweo akhoza kudzalandira mvula yoposera mlingo wa 250mm.

Mvula yokhazikika ikuyembezeka kugwa kuyambila sabata lachitatu la mwezi wa December.


## January 2026




Mlingo okhazikika kapena kuposela apo wapakati pa 250mm mpaka 300 mmm ukuyembekezeka m'mweziwu.
Komabe, madela ena ochepa ozungulira a kwa T/A Kawinga, T/A Liwonde, Liwonde National Park ndi Liwonde Town akuyembekezeka kulandila mvula yosaposela mlingo wa 250mm

Tiyembekezere Ng`amba yosapzola sabata limodzi mu mweziwu.


## February 2026




Mwezi wa February tiyembekezere mvula ya mlingo okhazikika m'madera ambiri yoyambila 150mm mpaka 200mm.
Komabe m'madera ena akhoza kudzalandira mvula yochepera mlingo okhazikika m'mweziwu.
Ng'amba yosapzola sabata limodzi mu mwezi wa February 2026 ikuyembekezeka.


.

## March 2026




Madera ambiri akuyembekezela kulandila mvula yokhazikika ya pakati pa 150mm mpaka 200mm.

## April 2026





Mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuchepela apo yosapzola mlingo wa 50mm yikuyembekezeka m'madela ambiri.

Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzafika kumapeto msabata loyambilila la mwezi wa April.

Mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuchepela apo ikuyembekezeka ku machinga mu dzinjali.

Mvula yokhazikika ikuyembekezeka kugwa kuyambila sabata lachitatu la mwezi wa December 2025
Nyengo ya mvula ikuyembekezeka kufika ku mapeto m'sabata loyamba la mwezi wa April 2026.

| NTAJA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 9.8 | 44.6 | 13.4 |
| NOV | 66.6 | 123.2 | 54.7 |
| DEC | 182.7 | 319.5 | 221.7 |
| JAN | 270.9 | 432.1 | 193.5 |
| FEB | 163.6 | 252.1 | 164.1 |
| MAR | 127.6 | 199.3 | 156.0 |
| APR | 10.8 | 59.2 | 29.2 |





**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2025**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: